# ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'DZINJA LA 2026 – 2027

**UNDUNA WA ZACHILENGEDWE**

Nthambi Yoona za Nyengo ndi Kusintha kwa Nyengo

UNITY AND FREEDOM

## NTCHEU

DISTRICT

## Mwachidule

Nyengo ya dzinja ya 2026-2027 ikuyembekezeka kukhudzidwa ndi El Niño wa mphamvu. El Niño ndi kutentha kopyola muyezo kwa madzi m'dera la pakati chakum'mawa kwa nyanja yamchere ya Pacific zomwe zimakhudza kagwedwe ka mvula dziko lonse.

Boma la Ntcheu likuyembekezeka kulandira mvula ya mlingo okhazikika kapena kuchepera apo mu nyengo ya dzinja ya 2026-2027.

## October 2026




Madera ambiri m'bomali kudzakhala kopanda mvula mu mweziwu. Komabe, madera ena akuyembekezeka kulandira mvula ya chizimalupsa yosaposera 30mm.

Mvulayi ikuyembekezeka kukhala ya mphepo ya nkuntho ndi ziphaliwali.

## November 2026




Madera ambiri akuyembekezeka kulandira mvula ya mlingo wa pakati pa 20 ndi 70mm.

Mvula yodzakhazikika ikuyembekezeka kudzayamba m'sabata lomaliza la mwezi wa November 2026.

## December 2026




Mu December, madera ambiri akuyembekezeka kulandira mvula yochuluka ya mlingo wa pakati pa 170-250mm. Komabe, madera ozungulira SC Makwangwala akuyembekezeka kulandira mvula ya mlingo wokwana 140mm.

## January 2027




Mwezi wa January , madera ambiri ku Ntcheu akuyembekezeka kulandira mvula ya mlingo wa pakati pa 140mm ndi 240mm.

Ng'amba yosaposera sabata imodzi ikuyembekezeka mu mweziwu.

## February 2027




Madera ambiri m'bomali adzalandira mvula yochepa ya mlingo wa pafupifupi 150mm.

Pali chiopsezo cha ng'amba yoposera ma sabata awiri mu mweziwu.

## March 2027




M'mweziwu boma la Ntcheu likuyembekezeka kulandira mvula ya mlingo wa pakati pa 120-200mm. Koma Madera ozungulira TA Mpando, SC Champiti ndi Ntcheu Boma akuyembekezeka kulandira mvula yochulukirapo ya mlingo oposera 220mm.

## April 2027




Nyengo ya mvula ikuyembekezeka kufika kumapeto kuyambira sabata loyamba Kapena lachitatu la mwezi wa April madera ambiri, ndipo madera ambiri akuyembekezeka kudzalandira mvula yosaposera 100mm.

## DZINJA MWACHIDULE

| Kuyamba kwa mvula yokhazikika | Ngamba | Kutalika kwa nyengo yadzinja | Mathero a mvula dzinja |
|---|---|---|---|
| Ikuyembekezereka sabata lachiwili mu December 2026 | Chiopyezo cha ng'amba ya sabata limodzi mu January komanso masabata awiri mwezi wa February | Dzinja lidzakhala masiku apakati pa 120 ndi 135 | Sabata lachiwiri Kapena la chitatu la mwezi wa April 2027 |

| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
|---|---|---|---|
| OCT | 4.4 | 29.4 | 33.5 |
| NOV | 51.7 | 71.8 | 64.0 |
| DEC | 147.0 | 262.8 | 258.6 |
| JAN | 219.4 | 315.3 | 205.0 |
| FEB | 198.3 | 261.3 | 144.2 |
| MAR | 148.7 | 189.6 | 254.9 |
| APR | 13.6 | 40.4 | 38.4 |




Chithunzi ichi chapereka dondomeko ya kagwedwe ka mvula ya pamwezi

Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku:

ActionFirst, WISER, WFP World Food Programme, The Development Fund, Save the Children, IOM UN MIGRATION, THE WORLD BANK, Malawi Red Cross Society, World Vision, NCA DCA actalliance, UK International Development (Partnership | Progress | Prosperity)

**Tsatilani ulosi ndi malangizo ochokera ku nthambi yoona zanyengo**


**For further information contact:**

The Director of Climate Change and Meteorological Services,
P.O. Box 1808, Blantyre.

+265 991 69 00 61
metdept@metmalawi.gov.mw
www.metmalawi.gov.mw